# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO


### ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA NTCHISI M'DZINJA LA 2024-2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE

Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.

Boma la Dowa likuyembekezera kulandira mvula yA **mlingo wokhazikika**.


## October 2024




M'mwezi wa October, madera ambiri adzalandira mvula yochepera 50mm. Mlingo wu ndi wokhazikika m'mwezi wa October m'bomali.

Mphepo yamkutho chifukwa chakutetha ikuyembekezeka mwezi wu.


## November 2024




M'mwezi wa November, madera ambiri akuyembekezeka kulandila mvula ya mlingo wapakati pa 50mm ndi 100mm. Komabe, mvula ikuyembekezeka kuyamba **pakati pa sabata lachinayi la November ndi sabata ya chiwili la December.**

Tiyembekezerenso mphepo yamkutho komanso mphezi.


## December 2024




Madera ambiri akuyembekezeka kudzalandila mvula yapafupifupi 200mm. Komabe, madera 0chepa aku mpoto kwa SC Kayembe akuyembekezeka kudzalandila mvula yopitilila 200mm.


**Sabata ya chiwiri ya December mvula ikuyembekezeka kuyamba m'madera ambiri m'boma la Dowa**.

## January 2025





Ulosi ukusonyeza mvula ya mlingo wokhazikika madera ambiri. Madera apakati kwa TA Chiwere akuyembekezeka kulandila mulingo wa mvula opitilila 300mmm. Ng'amba yapafupifupi sabata ikuyembekezeka m'mweziwu makamaka madera ena omwe akuyembekezeka kulandila mvula yochepera mlingo okhazikika monga SC Mponela, TA Dzoole and SC Chakhaza.

## February 2025




mvula yochepa ikuyembekezeka kugwa makamaka madera akumwera kwa TA Dzoole, SC Kayembe komanso madera ena a kwa SC Mponela. Maderawa akuyembekezeka kulandila mvula ya mlingo wa pakati pa 100mm ndi 150mm. Madera ena apakati kwa TA Chiwere akuyembekezeka kulandila mbvula ya mlingo wapafupifupi 250mm.
Tiyembekezere ng'amba yapafupifupi sabata limodzi m'wezi wa February.


## March 2025




Mvula ya mlingo opitilila mlingo okhazikika ikuyembekezeka kugwa madera ambiri.

Madera ambiri akuyembekezeka kulandila mbvula yapakati pa 100mm ndi 200mm.

## April 2025





Nyengo ya dzinja ikuyembekezeka kutha pakati pa sabata ya chitatu la mwezi wa March ndi sabata la chiwiri la mwezi wa April.

Komabe, pali kuthekera kuti madera ena akuyembekezeka kudzalandila mvula pafupifupi 50mm kapena kupitilila.

*Boma la Dowa likuyembekezeka kulandira mvula **mlingo wokhazikika m'dzinja la 2024-2025**. Mvula ikuyembekezeka kuyamba pakati pa sabata la chinayi la November ndi sabata la chiwiri la December 2024 ndikutha pakati pa sabata la chinayi la mwezi wa march ndi sabata la chiwiri la April 2025. Nyengoyi ikuyembekezeka kukhala pakati pa masiku 110 mpaka 140. Pali kuthekera kwakukulu kokhala ndi ng'amba yomwe ikuyembekezeka yapafupifupi sabata imodzi m'mwezi wa February. Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ku Dowa yaperekedwa pansipa;*

| DOWA | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0.0 | 2.6 | 4.8 |
| NOV | 23.7 | 42.8 | 19.6 |
| DEC | 142.0 | 193.9 | 208.8 |
| JAN | 191.0 | 294.0 | 253.7 |
| FEB | 151.0 | 245.2 | 207.1 |
| MAR | 117.2 | 202.1 | 183.4 |
| APR | 17.3 | 43.0 | 43.8 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: